



163 مَدَنِي پھول (CHICHEWA)

# NGALE 163 ZA MADANI



Lamasulidwa  
m'chichewa ndi

Oyambitsa

Sheikh-e-Tariqat Amir-Ahl-e-Sunnat il fondatore di  
DawatIslami Allama Moulana Abu Bilal

**MUHAMMAD ILYAS**  
Attar Qadiri Razavi رحمۃ اللہ علیہ

163 مدنی پھول

163 Madani Phool

## NGALE 163 ZA MADANI

Bukuli linalembedwa ndi Shaykh-e-Tareeqat, Ameer-e-Ahle-Sunnat, amene muyambisi Dawat-e-Islami ‘Allamah Maulana Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qadiri Razavi mu **دَاوَاتِ بَرَكَاتِهِمُ الْعَالِيَةِ**. **Nthambi yomasulira** lamasulira bukuli muchichewa. Ngati mungapeze cholakwika mumamasuliridwe kapena kafotokozedwe, chonde dziwitsani nthambi yomasulira pa keyala kapena imelo iyi ndi cholinga choti mulandire mphoto [Sawab].

### **Nthambi yo masulira (Dawat-e-Islami)**

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagran,  
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

**UAN:** ☎ +92-21-111-25-26-92 – Ext. 7213

**Email:** ✉ translation@dawateislami.net

**Ngale 163 za Madani**  
Kumasulira Mchichewa kwa 'Ngale 163 Madani'



**UFULU WONSE WASUNGIDWA**

© 2023 Maktaba-tul-Madinah

Palibe gawo lililonse la bukuli lomwe liriloredzedwa kutulutsidwa, kapena kutumizidwa, munjira ina iliyonse, kapena mwanjira iliyonse, zamagetsi, kuchulukitsa, kujambula kapena mwina mulimonse, popanda chilolezo cholembedwa ndi Maktaba-tul-Madinah.

**Kusindikiza koyamba:** Rabi<sup>3</sup>-ul-Awwal, 1444 AH – (Sep, 2023)  
**Wosindikiza:** Maktaba-tul-Madinah  
**Kuchuluka:** -  
**ISBN:** -

**THANDIZO**

Chonde khalani omasuka potipeza ngati mukufuna kuthandiza kusindikiza kabuku kapena buku la chipembezo kuti likhale Isal-e-Sawab ya abale anu omwalira.

**Maktaba-tul-Madinah**

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah Mahallah Saudagran,  
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

**Email:** [global@maktabatulmadinah.com](mailto:global@maktabatulmadinah.com) | [feedback@maktabatulmadinah.com](mailto:feedback@maktabatulmadinah.com)

**Phone:** +92-21-34921389-93

**Web:** [www.dawateislami.net](http://www.dawateislami.net) | [www.maktabatulmadinah.com](http://www.maktabatulmadinah.com)

الْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى سَيِّدِ الْمُرْسَلِينَ  
أَمَّا بَعْدُ فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

## Du'a yowerengera bukuli

**W**erengani Du'a yotsatilayi (Pempho) musanayambe kuwerenga buku lililonse la chipembezo, mudzakumbukira chilichonse chomwe mudzawerenga, **لَنْ** بِشَاءَ اللَّهُ عَزَّ وَجَلَّ:

اللَّهُمَّ افْتَحْ عَلَيْنَا حِكْمَتَكَ وَأَنْشُرْ  
عَلَيْنَا رَحْمَتَكَ يَا ذَا الْجَلَالِ وَالْإِكْرَامِ

### Kumasulira

E Allah **عَزَّ وَجَلَّ** Titsekulireni makomo amaphunziro komanso mzeru zakuya, ndipo mutichitile chifundo, E! inu amene muli waulemelero komanso wolemekezeka.

(Al-Mustatraf, vol. 1, p. 40)

**Dziwani:** Mfunireni zabwino (Salat) mneneri wokonededwa **ﷺ** kamodzi kumayambiliro komanso kumapeto kwa Du'a.

## ZAMKATIMU

NGALE 163 ZA MADANI.....	1
Kupambana komfunira zabwino mtumiki ﷺ .....	1
Ngale 13 za Madani pakumwa madzi .....	2
Ngale 15 za Madani pakuyenda .....	6
Ngale 19 za Madani popaka mafuta ndi kupesa tsisi .....	11
Ngale 22 za Madani za tsitsi ndi kutsanzira Sunnah yakakongoletsedwe ka tsitsi ndi zina.....	19
Ngale 14 za Madani povala.....	25
Ngale 17 za Madani zokhudza ‘Imamah (chilemba) .....	29
Chonde <b>werengani</b> mfundo 6 za a zaumoyo zakupindulitsa kwa ‘Imamah .....	33
Ngale 19 za Madani zokhudza mphete .....	35
Ngale 20 za Madani zokhudza Miswak (Mswachi wantengo).40	
Ngale 16 za Madani Poyendera manda.....	45

الْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى سَيِّدِ الْمُرْسَلِينَ  
أَمَّا بَعْدُ فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ ط

## NGALE 163 ZA MADANI

Ngakhale Satana ayesetse motani kukupangitsani kuchita ulesi, werengani bukuli ndi kumalizilatu. **إِنَّ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ** mukatero, mudzaphunzira ma Sunnah ambiri.

### Kupambana komfunira zabwino mtumiki ﷺ

Mtumiki wolemekezeka ndi wodziwika **صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ** anati, ‘Anthu inu! Mosakayikitsa, kuchokera ku mantha ndi kuyankha mlandu pa tsiku la chiweruzo, munthu amene angapeze mwachangu chipulumutso adzakhala m’modzi wa inu amene wandifunira ine zabwino mochuluka padziko’. (*Al-Firdaus bima Soor-il-Khattab, vol. 5, tsamba. 277, Hadith 8175*)

صَلُّوا عَلَيَّ الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيَّ مُحَمَّدٍ

Tsono, nazi zina mwa Ngale za Madani zogwirizana ndi mitu yosiyanasiyana. Musaganize kuti iliyonse ndi ngale za Madani pa zomwe zaikidwa mundandanda uli pansipa kukhala Sunnah ya okonedwa Mtumiki **صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ**. Kupatula ma Sunan, mawu amene ananenedwa ndi owopa mulungu omwe analipo kale aphantikizidwanso momwemu. Kumbukirani lamulori,

palibe ntchito yomwe ingalengezedwe kukhala ‘Sunnah ya Mtumikil صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ pokhapokha itaziwika ndithu.

Msilamu wina aliyense atha kuchita ngale za Madani zili mkati mwa kabukuka ndi kukhala ndi chiyembekezo chopeza paradiso pochita ma sunnah. Abale ndi alongo a chisilamu olalikira onse akupemphedwa kuti asanapereke ulaliki wolimbikitsa ma sunnah, chonde werengani mutu wina uliwonse wangale za Madani mukabukuka malingana ndi nyengo yanu. Komanso werengani mizere yomwe yatchulidwa poyambilira ndi pamapeto pa mutu uliwonse.

Okonedwa abale a Chisilamu! Pomaliza, ndikutengerapo mwayi uwu kutchula kupambana kwa Sunnah odala komanso ena mwa ma Sunan komanso makhalidwe. Mtumiki wa chifundo, opembedzera Ummah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ananena kuti, ‘aliyense okonda Sunnah yanga, akonda ine, ndipo aliyense okonda ine adzakhala ndi ine mu Jannah.’ (*Ibn-e-‘Asakir, vol. 9, tsamba. 343*)

*Upangeni mtima wanga kukhala mzinda wa Sunnah zanu  
Ndipo kujanna zandipangeni kukhala moyandikana nanu E inu  
Mtumiki (صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ)*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ

## Ngale 13 za Madani pakumwa madzi

Mawu awiri odalitsika wonenedwa ndi mtumiki okonedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ

1. Osamwa [madzi] mumpweya umodzi (mosapumila) ngati ngamira. Koma mmalo mwake, imwani mu mpweya uwiri kapena utatu. Werengani (بِسْمِ اللَّهِ) musanamwe ndipo pamene mwamaliza kumwa, werengani (الْحَمْدُ لِلَّهِ).

*(Sunan-ut-Tirmizi, vol. 3, tsamba. 352, Hadith 1892)*

2. Mtumiki wopambana kwambiri صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ analetsa kupumira mpweya kapena kuwuzira mu chiwiya.

*(Sunan Abi Dawood, vol. 3, tsamba. 474, Hadith 3728)*

Pothirira ndemanga pa zonedwa kale mu Hadith yodaliska, othilira ndemanga odziwika, oganiza kwambiri za Ummah, Mufti Ahmad Yar Khan رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ ananena kuti: kupumira mu chidebe ndi chithu chochitidwa ndi nyama, komanso, siyani kamwa lanu patali ndi tambula pamene mukupuma pakuti mpweya ndi poizoni nthawi zina (mwachisanzo siyani tambula patali ndi kamwa pamene mukutulutsa mpweya). Osauzira tiyi kapena mkaka otentha kuti zizizire, koma dikirani kanthawi, akayamba kuzizira pang'ono, ndeye imwani.

*(Mirat-ul-Manajih, vol. 6, tsamba. 77)*

Komabe, palibe choipa kuuzira pa madzi mutatha kumufunira zabwino mtumiki ndi zina zotero. Ndicholinga chopeza machiritso.

3. Nenani. (بِسْمِ اللَّهِ) musanamwe madzi.
4. Imwani pang'ono pang'ono pamene mukumwa madzi,



kumwa mofulumira kumayambitsa nthenda ya chiwindi.

5. Imwani madzi modukizadukiza katatu.
6. Imwani madzi pogwiritsa tchito dzanja lamanja, komanso chokhala.
7. Imwani madzi otsala mu kapu mutatha kuchita Wuzu (ukhondo)Madziwa ndi machilitso a matenda 70, (chimodzimodzi ngati madzi a Zamzam chifukwa nawonso ndi machilitso ku Matenda ochuluka) kupatula ziwirizi, (mwachisanzo madzi osala ku wuzu ndi madzi a Zamzam) kumwa madzi aliwonse utayimilira ndi Makruh. (*Kuchokera mu: Fatawa Razawiyyah, vol. 4, tsamba. 575 ; vol. 21, tsamba. 669*)

Imwani madzi otsala ku wuzu komanso madzi a Zamzam choyimilira komanso choyang`ana ku Qiblah.

8. Onetsetsani kuti palibe chowononga chilichonse ndi zina zotero muchakumwa (madzi ndi zina zotero) musanamwe. (*Ithaf-us-Sadah vol. 5, tsamba. 594*)
9. Mukatha kumwa madzi, nenani kuti (أَلْحَمْدُ لِلَّهِ).
10. Hujjat-ul-Islam Sayyiduna Imam Muhammad Bin Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ ananena: werengani (بِسْمِ اللَّهِ). musanayambe kumwa [madzi], (أَلْحَمْدُ لِلَّهِ) pamapeto pa kupuma koyamba (أَلْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ), pa

mapeto pa kupuma kachiwiri komanso pa mapeto pakupuma kwa chitatu. (*Ihya-ul-'Uloom, vol. 2, tsamba. 8*)

11. Madzi akumwa oyera otsala a Msilamu mu tambula sakuyenera kutayidwa mosafunikira chifukwa atha kugwiritsadwanso ntchito.
12. Zafotokozedwa kuti ‘سُورَةُ الْمُؤْمِنِينَ شِفَاءٌ’, Chakudya kapena chakumwa chotsalira cha Msilamu ndi machilitso. (*Al-Fatawa Al-Faqihi-tul-Kubra li Ibn Hajar AlHaytami, vol. 4, tsamba. 117; Kashf-ul-Khifa, vol. 1, tsamba. 384*)
13. Pakapita mphindi imodzi mutamwa madzi, ngati muona madotho ochepa a madzi mu tambula, imwaninso amenewo.

Kuti muphunzire ma Sunnah zikwi pa mitu yosiyana siyana, gulani ndi kuwerenga ma buku a *Bahar-e-Shari'at* gawo 16, buku lamasamba 312, ndi *Sunnatayn aur Adaab*, buku la masamba 120, losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah. Imodzi mwanjira zabwino kwambiri zophunzirira ma Sunnah ndi kuyenda ndi ma Qafilah a Madani a Dawat-e-Islami pamodzi ndi odzipereka a mtumiki okonededwa.

*yendani ndi Qafila kuti mupeze Madalitso*  
*yendani ndi Qafila kuti muphunzire ma Sunnah*  
*yendani ndi Qafila ndipo mavuto anu adzatha*  
*yendani ndi Qafila mayeselo anu adzatha*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ      صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Okonedwa abale a Chisilamu! Pomaliza, ndikutengerapo mwayi uwu kutchula kupambana kwa ma Sunnah odala komanso ena mwa ma Sunan ndi makhalidwe. Mtumiki wa chifundo, صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ananena kuti, ‘aliyense okonda Sunnah yanga, akonda ine, ndipo aliyense okonda ine adzakhala ndi ine mu Jannah.’ (*Ibn-e-‘Asakir, vol. 9, tsamba. 343*)

*upangeni Mtima wanga kukhala mzinda wa Sunnah zanu bwana  
ku Jannah zandipangeni kukhala moyandikana nanu*

## Ngale 15 za Madani pakuyenda

1. Allah عَزَّوَجَلَّ Anati mu Surah Bani Israel, gawo 15, Ayah nambala 37:

وَلَا تَمْشِ فِي الْأَرْضِ مَرَحًا إِنَّكَ لَنْ تَخْرِقَ الْأَرْضَ وَلَنْ تَبْلُغَ الْجِبَالَ  
طُولًا

*Ndipo musayende padziko modzitukumula ; ndinthu, inu  
simungang’ambe nthaka ndiponso, simungalifikire Phiri  
m’kotalika.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Qur’ani)] (Gawo 15, Surah Bani Israel, Ayah 37)*

2. Mawu onunkhira onenedwa ndi mneneri okonedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ zinanenedwa pa tsamba 435 la Bahar-e-Shari’at, voliyomu 3, lamasamba 1197- lofalitsidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yosindikiza la Dawat-e-

Islami: Munthu wamamuna okutidwa ndi nsalu ziwiri anali wodzikuzwa komanso wonyada modzitukumula. Iye anamizidwa munthaka, ndipo akhala akumizidwabe mpaka tsiku lachiweruzo. *(Sahih Muslim, tsamba. 1156, Hadith 2088)*

3. Mtumiki Okondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ nthawi zina amatha kugwira dzanja la otsatira wake aliyense ndi dzanja lake lodala poyenda. *(Al-Mu'jam-ul-Kabeer, vol. 7, tsamba. 277, Hadith 7132)*
4. Nthawi zina Mtumiki oyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ amatha kuyenda mopendeketsa mutu kutsogolo pang'ono ngati iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anali kutsika kuchokera pa mwamba.  
*(Shumaaail-ul-Muhammadiyah lit-Tirmizi, tsamba. 87, Raqm 118)*
5. Osayenda monyada, kuvala ma tcheni a golide kapena chitsulo china chilichonse m'khosi mwanu, komanso mabatani akutsogolo [a Malaya] wotsegula ngati kudzionetsera. Awa ndi machitidwe awopanda mzeru, wodzikuzwa, ndi wolakwika. Ndi Haraam kuti amuna azivala zibangiri ndi ma tcheni a golide mukhosi. Kuvalanso zithu zina za chitsulo ndi kosaloredwa.
6. Ngati palibe choletsa, yendani kumbali ya njira pa liwilo lochepa. Osamathamanga kwambiri kotero anthu amayamba kukuyang'ana kuganiza ukupita kuti mwa changu chonchi. Osayenda pang'onopang'ono mwina anthu angaganize kuti ukudwala. Munthu sakuyenera kugwira dzanja la mnyamata wokongora, chifukwa kugwira kapena kugwirana chanza kapena kukumbatirana

ndi m`bale wina aliyense wa chisilamu kuchokera ku chilako lako ndi Haraam ndipo ndi mchitidwe okutsogolera ku gehena.

7. Sisunnah kuyang`ana uku ndi uko mosafunikira pamene mukuyenda. Yendani mwaulemu ndi maso anu atatsitsidwa. Sayyiduna Hassaan Bin Abi Sinaan رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anapita ku Eid Salah. Pamene iye رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ atabwerera kunyumba, mkazi wake anamufunsa: Ndi akazi angati omwe mwawaona lero? Iye رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anakhala chete. Pamene anakakamira, iye رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anati: ndinali kuyang`ana zala zanga (za kumapazi) kuchokera pamene ndinatuluka mnyumba mpaka kubwelera Kwanga Kwa inu. (*Kitab-ul-Wara` ma` Mawsu`ah Imam Ibn Abid Dunya, vol. 1, tsamba. 205*)

شَهِدَ اللَّهُ! Iwo oyera odala رَحْمَةُ اللَّهِ sanayang`ane uku ndi uko mosafunikira pamene amayenda, maka maka pamene pali gulu lodzaza, kuopa kuti angayang`ane pa wina wosaloredwa ndi Shari`ah kuyang`ana. Uku kunali kuopa Mulungu kwa anthu oyera رَحْمَةُ اللَّهِ. Lamulo ndiloti ngati kuyang`anitsitsa kwanu kwagwera mkazi mosadziwa ndipo mwapewa kuyang`ana kwanu nthawi yomweyo, simudzakhala ochimwa.

8. Sikoyenera kuyang`ana khonde kapena zenera la nyumba ya munthu wina mosafunikira.
9. Pakuyenda, kukwera kapena kutsika masitepe, samalitsani kuti nsapato zanu zisamamveke phokoso. Mtumiki wathu

wokonedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ sanakonde kumva phokoso lopangidwa ndi nsapato.

10. Ngati pali azimayi awiri ayima kapena akuyenda mu mseu, musadutse pakati pawo. Zinaletsedwa mu Hadith yodala. *(Abu Dawood, vol. 4, tsamba. 470, Hadith 5273)*
11. Ndizosemphana ndi chikhalidwe pa kulavula, kuliza mphuno, kuyika chala chanu mkati mwa mphuno, kuchotsa litsilo pa thupi lanu, kukanda makutu anu kapena malo obisika ndi zina Zotero pogwiritsa ntchito zala zanu pamene mukuyenda, mwakhala pansu kapena kuyima pa gulu la anthu
12. Anthu ena ali ndi chizolowezi choponya chilichonse chobwera pa njira yawo. Awa ndi machitidwe oyipa kwambiri. Palinso chiopsezo choti phanzi lanu litha kuvulala. Kuonjezera apo kukankha manyuzipepala, makatoni, majumbo ndi mabotolo opanda kanthu a madzi okhala ndi zolembedwa paiwo ndi kupanda ulemu kwakukulu.
13. Pamene mukuyenda, tsatani malamulo omwe samatsutsana ndi Shari'ah. Mwa chitsanzo, pomwe magalimoto akuyenda, ngati pamalo owolokera kapena mlatho wa pamwamba ulipo, gwilitsani ntchito izi pofuna kuwoloka mseu.
14. Wolokani msewu poyang'ana komwe magalimoto

akuchokera. Ngati muli pakati pa mseu ndipo galimoto yayandikira, m`malo moti muthamange, yesetsani kukhala pomwepo poti amenewo ndi malo otetezeka. Kuphatikiza apo, kuwoloka njanji nthawi yomwe sitima zimadutsa, nthawi zambiri kuli ngati kuziyitanira imfa. Yemwe akuganizira kuti sitima ili patali kwambiri ndi kuwoloka njanji ayenera kukumbukira kuopsa kokodwa muwaya ndi zina zambiri, ndi kugwa chifukwa chothamangira kapena kusasamala ndi kuphwanyidwa ndi sitima. Pali malo ena ndi kuphwanya lamulo kuwoloka njanji. Tsatani malamulowa makamaka m`malo mokwerera.

15. Yendani kwa mphindi 45 uku mukuchita Zikr ndi kumfunira zabwino mtumiki tsiku lililonse ndi cholinga chopeza mphamvu zolambira. **إِنَّ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ**, mudzakhalabe ndithanzi.

Njira yabwino poyenda ndi kuyenda mwa changu kwa mphindi 15 zoyamba, pango`no pang`ono kwa mphindi 15 zotsatira kenako mwachangunso mphindi 15 zomaliza. Poyenda chomwechi, thupi lonse lilimbikitsika. **إِنَّ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ**, Iyinso ndi njira yabwino yogayira zakudya imakhalanso bwino, muzakhala otetezedwa ku kudzimbidwa, gasi, kulemera kwambiri, matenda a mtima ndi matenda ambiri osawerengeka. **إِنَّ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ**

Kuti muphunzire ma Sunnah zikwi pa mitu yosiyana siyana, gulani ndi kuwerenga ma buku a *Bahar-e-Shari'at* gawo 16,

buku la ma samba 312, ndi *Sunnatayn aur Adaab*, buku la masamba 120, losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah. Imodzi mwanjira zabwino kwa mbiri zophunzirira ma Sunnah m’kuyenda ndi Madani Qafilah ya Dawat-e-Islami pamodzi ndi odzipereka a mtumiki okonedwa.

*yendani ndi Qafila kuti mupeze Madalitso*  
*yendani ndi Qafila kuti muphunzire ma Sunnah*  
*yendani ndi Qafila ndipo mavuto anu adzatha*  
*yendani ndi Qafila mayeselo anu adzatha*

Okonedwa abale a Chisilamu! Pomaliza, ndikutengerapo mwayi uwu kutchula kupambana kwa ma Sunnah odala komanso ena mwa ma Sunan ndi makhalidwe. Mtumiki wa chifundo, صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ananena kuti, ‘aliyense okonda Sunnah yanga, akonda ine, ndipo aliyense okonda ine akhala ndi ine mu Jannah.’ (*Ibn - e - Asakir, vol. 9, tsamba. 343*)

*upangeni Mtima wanga kukhala mzinda wa Sunnah zanu bwana*  
*ku Jannah zandipangeni kukhala moyandikana nanu*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ

## Ngale 19 za Madani popaka mafuta ndi kupesa tsisi

1. Sayyiduna Anas رَضِيَ اللهُ عَنْهُ ananena kuti mtumiki wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ thawi zambiri amapaka



mafuta m'mutu odala ndi kupesa ndevu zodala ndipo iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ thawi zambiri amayika ka nsalu (Sarband wolemekezeka) pamwamba pa mutu odala, mpaka kufikira nsalu imanyowa ndi mafuta. (*Ash-Shumaaail-ul-Muhammadiyah, tsamba. 40, Hadith 32*)

Kuchokera apa, timadziwa kuti kugwiritsa ntchito 'Sarband ndi Sunnah. Abale achisilamu ayenera kuvala ka nsalu pa mutu wawo nthawi iliyonse apaka mafuta mutu wawo, mwa ichi, إِنَّ شَاءَ اللهُ عَزَّوَجَلَّ chipewa ndi nduwira zimakhala zotetezedwa ku mafuta ochuluka kwambiri. اَلْحَمْدُ لِلَّهِ عَزَّوَجَلَّ, Sag-e-Madinah عُقْبَى عَنْهُ wakhala akugwiritsa ntchito sarband pafupi pafupi ndi cholinga chochitapo kanthu pa Sunnahyi kwa zaka zambiri.

2. Kunena kwa mtumiki wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ: Aliyense ali ndi tsitsi alilemekeze. (*Sunan Abi Dawood, vol. 4, tsamba. 103, Hadith 4163*) monga atsuke, apake mafuta, ndipo apese. (*Ashi'a-tul-Lam'aat, vol. 3, tsamba. 617*)

Fungo loipa nthawi zambiri limachokera ku tsitsi la iwo omwe samatsuka tsitsi ndi ndevu zawo ndi sopo ndi zina zotero, ngakhale iwo eni samazindikira izi koma ena amatha kuzimva. Ndi Haraam (choletsedwa) kulowa mu Masjid ndi fungo loyipa lochokera mkamwa, mtsitsi, mthupi ndi zovala komanso zina ndi zina, chifukwa Angalo amanyasidwanazo komanso kubweretsa mavuto kwa anthu.

3. Sayyiduna Naafi' رَضِيَ اللهُ عَنْهُ wanena kuti: Sayyiduna Ibn 'Umar رَضِيَ اللهُ عَنْهُمَا amagwiritsa ntchito mafuta [tsitsi lake]

kawiri pa tsiku. (*Musannaf Ibn Abi Shaybah, vol. 6, tsamba. 117*)

Tsitsi kulipaka mafuta pafupi pafupi ndikothandiza maka maka kwa ophunzira kukhala opanda mfundu, kutsitsimutsa ubongo ndi kulimbikitsa kukumbukira mwachangu.

4. Kunena kwa mtumiki wokonedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ: Pamene wina wainu apaka mafuta, ayambe ndi nsidze, izi zimachepetsa matenda a mutu. (*Al-Jami'-us-Sagheer, tsamba. 28, Hadith 369*)
5. Zanededwa mu 'Kanz-ul-'Ummal': nthawi iliyonse Mtumiki wathu wokonedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ akapaka mafuta Amayamba kuthira pa chikhatho cha dzanja la mamzere, kenako ndi kupaka tsitsi la muzikope zodala, komanso maso onse odala [i.e. nsidze zake zodala] kenako mutu odala. (*Kanz-ul-'Ummal, vol. 7, tsamba. 46, Raqm 18295*)
6. Zanededwa mu Tabarani: Pamene Mtumiki wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ akapaka mafuta ndevu zodala, iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ amayamba ndi 'Anfaqah (mwachisanzo tsitsi lokula pakati pa mlomo wapansi ndi chibwano). (*Al-Mu'jam-ul-Awsat, vol. 5, tsamba. 366, Hadith 7629*)
7. Ndi Sunnah kupesa ndevu. (*Ashi'a-tul-Lam'aat, vol. 3, tsamba. 616*)
8. Ndikutsutsana ndi Sunnah kupaka mafuta popanda kunena. (بِسْمِ اللهِ) ndi kusunga tsitsi louma ndi losapesa.

9. Zanenedwa mu Hadith yodalitsika: Amene apaka mafuta popanda kunena (بِسْمِ اللَّهِ), a satana makumi asanu ndi awiri atsagana naye. (*Amal-ul-Yawm wal-Laylah, vol. 1, tsamba. 327, Hadith 173*)
10. Hujjat-ul-Islam Sayyiduna Imam Muhammad Bin Muhammad Bin Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anafotokoza: Sayyiduna Abu Hurayrah رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anati: kalekalero, Satana anatsogozana ndi msilamu weniweni ndipo anakumana ndi satana otsogozana ndi osakhulupirira. Ndiye Satana otsogozana ndi osakhulupirira anali wathanzi komanso ovala bwino, pamene Satana otsogozana ndi msilamu analibe mphavu, osavala ndipo tsitsi lake losapesa. Satana otsogozana ndi osakhulupira anafunsa satana otsogozana ndi msilamu: chifukwa ninji uli ofooka? Iye anayankha: ndimatsogozana ndi munthu amene amanena (بِسْمِ اللَّهِ) pamene akudya ndi kumwa choncho ine ndimakhala ndi njala komanso ludzu. Iye amanena (بِسْمِ اللَّهِ) pamene akupaka mafuta kotero tsitsi langa limasiyidwa losapesa. Pakumva izi, satana otsogozana ndi osakhulupirira anati: ine ndimatsogozana ndi munthu amene sapanga kalikonse [mwachisanzo sawerenga (بِسْمِ اللَّهِ)] pochita izi kotero ndimatenga naye gawo pakudya, kumwa (madzi ndi zina.), kuvala ndi kupaka mafuta. (*Ihya-ul-Uloom, vol. 3, tsamba. 45*)
11. Musanadzole mafuta, nenani (بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ) ndipo

pungulirani timafuta pa chikhatho cha dzanja lanu lamanzere choncho, koyamba pakani mafuta tsitsi la chikope cha diso lanu lakumanja, kenako diso lamanzere, kenako nsidze za diso lakumanja, kenako za diso lakumanzere, kenako pa kani mafuta tsitsi lonse. Ngati mukupaka mafuta pa ndevu, yambani ndi tsitsi limene limakula pakati pa mlomo wapansi ndi chibwano.

12. Iye amene amagwiritsa ntchito mafuta a nthanga za mpiru akavula chipewa kapena nduwira, nthawi zina fungo loyipa limatuluka. Choncho, aliyense angakwanitse, adzipaka mafuta wonunkhira m' mutu mwake. Njira yosavuta yopangira mafuta wonunkhira ndi kuwonjezera madontho amakonda anu 'onunkhira mu botolo la mafuta a kokonati ndi kusungunula, mafuta onunkhira ndi okonzeka kugwiritsa ntchito tsopano. Tsukani tsitsi la m' mutu komanso ndevu ndi sopo nthawi zonse.
13. Mzimayi akuyenera kubisa tsitsi lomwe lagwa popesa kapena potsuka, kuti pasapezeke mlendo (i.e. munthu amene mwa iye banja kapena ukwati siharaam nthawi zonse) asaliwone. (*Bahar-e-Shari'at, vol. 3, tsamba. 449*)
14. Mtumiki wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ analetsa kupesa tsitsi lililonse. (*Sunan-ut-Tirmizi, vol. 3, tsamba. 293, Hadith 1762*) Kuletsa uku ndi (Makruh) Tanzeehi ndipo cholinga chake ndikuti munthu asakhale otanganidwa ndi kuzikongoletsa. (*Bahar-e-Shari'at, vol. 3, tsamba. 592*)

Imam Manaawi رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ ananena kuti: ngati wina tsitsi lake ndi lochuluka chifukwa cha ichi atha kupesa tsiku lililonse ndithu. (*Fayd-ul Qadeer, vol. 6, tsamba. 404*)

15. Zanenedwa apa ndi funso ndi yankho lake lofunsidwa kwa mtsogoleri wa Ahl-us-Sunnah, Imam Ahmad Raza Khan رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ.

**Funso:** ndi nthawi yanji yomwe ndevu zikuyenera kupesedwa?

**Yankho:** palibe nthawi yeniyeni yopesa inayikidwa mu Shari'ah, zinalamulidwa kuti atsate zolimbitsa thupi, ngakhalenso mwamuna asazipange iye kuoneka mwachilendo kapena iye kukhalabe otangwanika ndi kuzikongoletsa yekha nthawi zonse. (*Fatawa Razawiyah, vol. 29, tsamba. 92, 94*)

16. Yamba kupesa mbali yakumanja. Umm-u-l-Mu`mineen, Sayyidatuna 'Aaishah Siddiqah رَضِيَ اللَّهُ عَنْهَا ananena: Mtumiki wolemekezeka صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ amakonda kuyamba kuchita zonse ndi mbali yakumanja; ngakhale povala msapato, popesa, ndi kupeza chiyero. (*Sahih Bukhari, vol. 1, tsamba. 81, Hadith 168*)

Wothirira ndemanga wa *Sahih Bukhari*, 'Allamah Badruddin 'Ayni Hanafi رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ walembe zokhudza Hadith iyi: zinthu zitatu izi zatchulidwa monga zitsanzo, kotero ndi zokonedwa kuyamba kuchita chilichonse cholemekezeka ndi cholungama ndi mbali yakumanja. Monga pakulowa mu Masjid, povala Zovala, kugwiritsa ntchito Miswak, kupaka kohl, kuwenga

zikhadabo ndi kuyepula masharubu, kumeta ku nkhwapa, kuchita Wudu (ukhondo) posamba, pochoka ku chimbudzi, ndi zina zotero. ndi machitidwe omwe Sali apadera ngati pochoka ku Masjid, polowa mu chimbudzi, pomina, povula zovala (Shalwar), ndi zokonedwa kuyamba mbali yakumanzere.

*(Umdatul-Qaari, vol. 2, tsamba. 476)*

17. Ndi zokonedwa kupaka mafuta ndi zonunkhiritsa popita ku salah ya Jumu'ah. *(Bahar-e-Shari'at, vol. 1, tsamba. 774)*
18. Sikoyipa kupaka mafuta pa ndevu ndi masharubu pamene mukusala kudya, komabe ngati wina apaka mafuta ndi cholinga cho kulitsa ndevu ngakhale zoonza zake iye ali ndi ndevu zazitali kale, ndi Makruh (chonyasa) ngakhale iye asakusala kudya, ndipo kuyipa kwake ndi kwakukulu ngati akusala kudya. *(Bahar-e-Shari'at, vol. 1, tsamba. 997)*
19. Ndikosavomerezeka ndinso tchimo kupesa tsitsi ndi ndevu za womwalira. *(Durr-e-Mukhtar, vol. 3, tsamba. 104)*

Anthu amameta ndevu za omwalira, izinso zosavomelezedwa ndinso tchimo. Omwalirayo sakhala ochimwa koma iwo amene amumeta kapena omwe alamula kuti ametedwe.

*E Raza! Awa simadontho a Mafuta,  
Amene akugwa kuchokera mu Tsitsi lake lopatulika  
Pamasaya ake a pinki, Nyenyezi zowala zikuwalitsa, pa Tsitsi lake  
lopatulika*

*(Hadaiq-e-Bakhshish)*

Kuti muphunzire ma Sunnah zikwi pa mitu yosiyana siyana, gulani ndi kuwerenga ma buku a *Bahar-e-Shari'at* gawo 16, buku lamasamba 312, ndi *Sunnatayn aur Adaab*, buku la masamba 120, losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah. Imodzi mwanjira zabwino kwambiri zophunzirira maSunnah ndi kuyenda ndi Madani Qafilahs a Dawat-e-Islami pamodzi ndi odzipeleka a mtumiki okondedwa.

*yendani ndi Qafila kuti mupeze Madalitso*  
*yendani ndi Qafila kuti muphunzire ma Sunnah*  
*yendani ndi Qafila ndipo Mavuto anu adzatha*  
*yendani ndi Qafila mayeselo anu adzatha*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ

Okondedwa abale a Chisilamu! Pomaliza, ndikutengelapo mwayi uwu kutchula kupambana kwa Sunnah yodala komanso ena mwa ma Sunan ndi makhalidwe. Mtumiki wa chifundo, opembedzera Ummah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ananena kuti, ‘aliyense okonda Sunnah yanga, akonda ine, ndipo aliyense okonda ine akhala ndi ine mu Jannah.’ (*Ibn-e-'Asakir, vol. 9, tsamba. 343*)

*upangeni Mtima wanga kukhala mzinda wa Sunnah zanu bwana*  
*ku Jannah zandipangeni kukhala moyandikana nanu*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ

## Ngale 22 za Madani za tsitsi ndi kutsanzira Sunnah yakakongoletsedwe ka tsitsi ndi zina

1. Zulf [tsitsi lalitali lopesedwa chogwira mbali] lamtumiki wolemekezeka  
صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ Nthawi zina limakhala theka la makutu odalitsika,
2. nthawi zina, kumakutu odalitsika
3. Ndipo nthawi zina, limafika ku mapewa odalitsika.

*(Shumaail-ut-Tirmizi, tsamba. 34, 35, 18)*

4. Nthawi ndi nthawi, tiyenera kuchitapo kanthu pa ma sunnah atatu awa. Kotero, nthawi zina, tiyenera kusunga Zulf yathu pansu mu theka la makutu, nthawi zina pa makutu, ndi nthawi zina pa mapewa.
5. Sunnah yosungira Zulf [Sunnah- ya kutsanzira makongoletsedwa a tsitsi] kufika mapewa nthawi zambiri imakhala yovuta ku mitima (Nafs) yathu. Komabe, aliyense ayenera kuchita Sunnah iyi osachepera kamodzi mmoyo mwake. Choncho, ndi kofunikira kusamalitsa kuti tsitsi lisamafike pansu pa mapewa. Kutalika kwa tsitsi kutha kuonekera bwino pamene tsitsi ndi lonyowa. Choncho m' masiku omwe tsitsi lakula kutenga mbali pa Sunnah iyi, pesani tsitsi mukatha kusamba ndipo onetsetsani bwino lomwe kuti tsitsi silikufika pansu pa mapewa.



6. A'la Hadrat mtsogoleri wanga رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ ananena kuti: ndi Haraam kuti abambo asunge tsitsi mpaka kufika pansu pamapewa, monga akazi achitira. (*Fatawa Razawiyyah, vol. 21, tsamba. 600*)
7. Katswiri odziwa komanso ophunzira otsogola wa Shari'ah ndi Tareeqah, 'Allamah Maulana Mufti Muhammad Amjad 'Ali A'zami رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ ananena: sizoloredwa kuti mwamuna akhale ndi tsitsi lalitali ngati mkazi. Anthu ena otchedwa anqwirowo amasunga tsitsi lalitali kwambiri lomwe limapachikidwa pa chifuwa pawo ngati njoka, ndipo ena mwa iwo amaluka tsitsi lawo mofanana ndiakazi. Zonsezi ndizosavomerezeka ndipo zotsutsana ndi Shari'ah. Zinsinsi za zikhulupiriro sizigona pa kukulitsa tsitsi ndi kuvala zovala zokongola, koma izi zagona pakumvera mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ kwathuthu ndikupereka nsembe zokhumba za mitima.  
(*Bahar-e Shari'at, vol. 3, gawo 16, tsamba. 587*)
8. Ndi Haraam kuti mkazi amete mutu wake.  
(*chidule cha Fatawa ya Razawiyyah, vol. 22, tsamba. 664*)
9. Musamete tsitsi la mwana wamkazi m' maonekedwe amphongo. Mupatseni malingaliro osunga tsitsi lalitali kuyambira mu umwana wake.
10. Anthu ena amapatula tsitsi kupita mbali ya manja kapena kumanzere. Izi zotsutsana ndi Sunnah.

11. Ngati wina ali ndi tsitsi m`mutu, ndi Sunnah kupatula kuyambira pakati. *(Bahar-e Shari`at, vol. 3, gawo 16, tsamba. 587)*
12. Mamuna ali ndi chisankho chometa mutu mwake kapena ayi ndi kupatula tsitsi.
13. Zonse ndizovomezedwa kuchokera kwa mtumiki wokondedwa. صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ Ngakhale kumeta kumavomezedwa pa nthawi yomwe mukuchotsa Ihram, osati nthawi Ina iliyonse. *(Bahar-e-Shari`at vol. 3 tsamba. 586)*
14. Masiku ano, tsitsi likumametedwa mmaonekedwe a chilendo, pogwiritsa tchito lumo kapena makina, ndikupanga mbali yina ya tsitsi kutalika ndi mbali yina lalifupi. Sisunnah kukhala ndi mametedwe amenewa.
15. Kunena kwa mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ : Aliyense ali ndi tsitsi apeleke ulemu kwa ilo (mwachisanzo: litsukeni, lipakeni mafuta ndi kulipesa). *(Sunan Abi Dawood, vol. 4, tsamba. 103, Hadith 4163)*
16. Sayyiduna Ibraheem Khaleelullah عَلَيْهِ الصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ anali woyamba kudula tsitsi la masharubu, ndi oyamba kuona tsitsi loyera. Iye عَلَيْهِ السَّلَامُ anati, ‘E Ambuye عَزَّوَجَلَّ! Kodi ichi ndi chiyani?’ Allah عَزَّوَجَلَّ ! anayankha, ‘E Ibraheem! Uwu ndiye ukulu wako.’ عَلَيْهِ السَّلَامُ kenako anati, ‘E mbuye wanga! Wonjezerani ukulu wanga.’ *(Muwatta, vol. 2, tsamba. 415, Hadith 1756)*

Otchuka Mufassir Hakeem ul ummat Hadrat Mufti Ahmed Yar Khan رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ akunena pa Hadith iyi: Pamaso pa iye (Sayyiduna Ibraheem Khaleelullah عَلَيْهِ الصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ) palibe masharubu a mneneri aliyense عَلَيْهِ السَّلَامُ anakula motalika ndi kudulidwa ndi iwo, koma sizinalamulidwe mu Shari'ah mwawo kudulira masharubu. Tsono chifukwa cha iye (Sayyiduna Ibraheem Khaleelullah عَلَيْهِ الصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ), mchitidwe uwu unakhala Sunnah yake.

17. sizili Sunnah kumeta kapena kudzula tsitsi kuchokera mu gawo la pakati pa mulomo wapansi ndi chibwano. (*Fatawa Aalamgiri, vol. 5, tsamba. 358*)
18. Ndi Makruh kumeta tsitsi la kumbuyo kwa khosi lametedwa. (*Ibid tsamba. 357*) koma zimatheka pamene wina wameta tsitsi kumbuyo kwa khosi koma osati tsitsi la mmutu. Monga anthu ambiri amameta tsitsi lakumbuyo kwa khosi pamene ndevu zawo zadulidwa munjira yovomerezeka mwa Sunnah. Ngati tsitsi lamutu onse lametedwa, choncho potsatana ndi izi, tsitsi la kumbuyo kwa khosi limetedwensho. (*Bahar-e Shari'at, vol. 3, gawo 16, tsamba. 587*)
19. Kwalamulidwa kukwilira zinthu zinayi izi, tsitsi, zikhadabo, kanutsu ka nsalu komwe mkazi amagwilitsa tchito kuziyeretsa magazi akusamba ndi mwazi.

(*'Aalamgiri, vol. 5, tsamba. 358*)

20. Ndi Mustahab kuti amuna asintha mtundu wa tsitsi loyera la ndevu ndi mmutu kukhala lofiira kapena la yelo m'maonekedwe. Pachifukwa ichi, Mehndi [henna] atha kugwilitsidwa ntchito.
21. Munthu sayenera kugona atapaka henna ku ndevu kapena tsitsi. Molingana ndi Hakeem [adotolo azitsamba], kugona mutatha kupaka henna mu njira iyi kutha kuyanbitsa vuto lamaso, izi zimaononga kapenyedwe ka maso. Malangizo awa a Hakeem [dotolo wazitsamba] anawunikiridwa motere munthu wakhungu anabwera kwa wokonda Madina [mwachisanzo Ameer-e-Ahl- e Sunnat دَاعَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَةِ] nthawi ina yake ndipo Iye anati, sanabadwe osopenya, koma zachisoni, anapaka henna ku tsitsi lake ndi kupita kukagona. Pamene iye anadzuka, anali atasiya kupenya kwake.
22. Kuyera kwa tsitsi la masharubu, mulomo wapansi, ndi m'mbali mwa ndevu mwa anthu amene amapaka henna kumaonekera patangopita masiku ochepa chabe ndipo izi siziwoneka bwino. Kotero, ngati sungathe kusintha mtundu wa ndevu mobwereza bwereza, choncho pakatha masiku anayi, kapena osachepera apa yesetsani kupaka mulingo pang'ono wa henna ku malo omwe kuyera kwayamba kuonekera.

Zanenedwa mu Sharh-us-Sudoor kuti Sayyiduna Anas رضي الله عنه ananena kuti: ‘iye amene amagwiritsa ntchito henna (mtundu wa utoto wa tsitsi ndi zina koma osati zakuda, monga zofiira kapena yelo) ku ndevu kwake, Munkar Nakeer sadzamufunsa iye atamwalira. Munkar adzanena kuti, “E Nakeer! Kodi ine ndifunsa bwanji munthu amene ali ndi noor (kuwala) kwa Chisilamu pa nkhope yake? (*Sharhus-Sudoor, tsamba. 152*)

Kuti muphunzire ma Sunnah zikwi pa mitu yosiyana siyana, gulani ndi kuwerenga ma buku a *Bahar-e-Shari’at* gawo 16, buku lamasamba 312, ndi *Sunnatayn aur Adaab*, buku la masamba 120, losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah. Imodzi mwanjira zabwino kwambiri zophunzirira ma Sunnah yendani ndi Madani Qafilah ya Dawat-e-Islami pamodzi ndi odzipereka a mtumiki wokonededwa. (صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ)

*yendani ndi Qafila kuti mupeze Madalitso*  
*yendani ndi Qafila kuti muphunzire ma Sunnah*  
*yendani ndi Qafila ndipo Mavuto anu adzatha*  
*yendani ndi Qafila mayeselo anu adzatha*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ      صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Okonededwa abale a Chisilamu! Pomaliza, ndikutengerapo mwayi uwu kutchula kupambana kwa ma Sunnah odala komanso ena mwa ma Sunan ndi makhalidwe. Mtumiki wa chifundo, opembedzera Ummah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ananena kuti, ‘aliyense okonda Sunnah yanga, akonda ine, ndipo aliyense

okonda ine adzakhala ndi ine mu Jannah.’ (*Ibn-e-‘Asakir, vol. 9, tsamba. 343*)

*upangeni Mtima wanga kukhala mzinda wa Sunnah zanu bwana  
ku Jannah zandipangeni kukhala moyandikana nanu*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

## Ngale 14 za Madani povala

Poyamba, zonedwa zitatu za mtumiki odalitsika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ zaperekedwa:

1. Chophimba pakati pa maso a ma jinn (ziwanda) komanso Satr (chophimba) cha anthu ndi pamene wina aliyense akuvula zovala, akuyenera kunena (بِسْمِ اللهِ).

*(Al-Mu’jam-ul-Awsat, vol. 2, tsamba. 59, Hadith 2504)*

Mufti Ahmad Yar Khan Na’eemi woganiza kwambiri za Ummah رَحِمَهُ اللهُ عَلَيْهِ anati, ‘monga khoma ndi nsalu zimakhala chotchinga pamaso pa anthu, momwemonso Zikr za Allah عَزَّوَجَلَّ zimakhala chotchinga ku kuona kwa ma jinni. Ndiye kuti, jinni sangakwanitse kuona (ziwalo zake zobisika). (*Mirat-ul-Manajih, vol. 1, tsamba. 268*)

2. Aliyense amene akuvala zovala zake ndi kuwerenga izi, machimo ake a mtsogolo ndi akale adzakhululukidwa:

الْحَمْدُ لِلَّهِ الَّذِي كَسَانِي هَذَا وَرَزَقَنِيهِ مِنْ غَيْرِ حَوْلٍ مِنِّي وَلَا قُوَّةٍ

*(Shu’ab-ul-Iman, vol. 5, tsamba. 181, Hadith 6285)*

3. Angakhale pali mwayi wotha kuvala zovala zapamwamba, aliyense amene amazipewa chifukwa chodzichepetsa, Allah ﷺ adzamuveka iye zovala zolemekezeka. (Karamah)  
*(Sunan Abi Dawood, vol. 4, tsamba. 326, Hadith 4778)*
4. Zovala zopatulika za mtumiki wolemekezeka ﷺ Zimakhala zovala za mtundu oyera. *(Kashf-ul-Iltibas, tsamba. 36)*
5. Zovala ziyenera kuchokera munjira ya Halal. palibe Salah ya Fard kapena Nafil izavomerezedwa ngati atavala zovala zomwe zapezedwa kudzera munjira ya Haraam.  
*(Kashf-ul-Iltibas, tsamba. 41)*
6. Zafotokozeredwa: aliyense amene amanga Imamah yake chokhala, kapena kuvala chovala chakumusi (monga kabudula kapena buluku) choyima, Allah ﷺ adzakupanga iye kuvutika ku matenda omwe alibe machilitso. *(Kashf-ul-Iltibas, tsamba. 39)*
7. Pamene mukuvala, yambani mbali yakumanja (chifukwa ndi Sunnah). Mwachitsanzo, pamene mukuvala Mkanjo, poyamba lowetsani dzanja lanu la manja mu mkono wakumanja ndipo kenako dzanja lanu la manzere ku mkono wakumanzere. *(Kashf-ul-Iltibas, tsamba. 43)*
8. Munjira yomweyi, povala chovala chakumusi, poyamba lowetsani phanzi lanu la manja ku mwendo wamanja ndipo kenako phanzi lanu la manzere ku mwendo wanu

wamanzere, ndipo pamene muvula zovala zanu, chitani mosemphana, monga, yambani ndi kumanzere.

9. Zanenedwa pa tsamba 409, voliyumu 3 la buku la Bahar- e Shari'at, la masamba 1197- losindikizidwa ndi Maktaba- tul-Madinah, nthambi yofalitsa la Dawat-e-Islami: ndi Sunnah kukhala ndi mkanjo wotalika mpaka pansa pa theka la mwendo, kutalika kwa manja mpaka kufika kufupi ndi zala, ndipo mulifupi mwake muyenera kukhala sayizi ya chikhatho chimodzi cha manja.

*(Rad-dul Muhtar, vol. 9, tsamba. 579)*

10. Ndi Sunnah kwa amuna malire a buluku lawo akhale pa mwamba pa misomali (akakolo). *(Mirat-ul-Manajih, vol. 6, tsamba. 94)*
11. Amuna avale zovala zachimuna ndipo azimayi avale zovala zachikazi. Kusiyanitsa uku kutengedwenso pamene tikuveka ana achichepere.
12. Zanenedwa pa tsamba 481, voliyumu 1 la Bahar-e-Shari'at, la masamba 1250 losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yofalitsa la Dawat-e-Islami: gawo la thupi la mwamuna kuchokera mchombo kufikira mmusi mwa mawondo ndi 'maliseche, chomwecho, kubisa izi ndi Fard (chikakamizo). Mchombo sukuphatikizidwamo koma mawondo akuphatikizidwa.

*(Durr-e-Mukhtar, Rad-dul-Muhtar, vol. 2, tsamba. 93)*



Masiku ano, anthu ambiri amavala buluku kapena Tahband (chilundu) mmusi mwa mchombo munjira yoti gawo lina muni mwa mchombo silibisidwa. Ngati nkanjo ndi zina zotero, muzibisa gawo limeneli mpaka kufikira kuti mtundu wa khungu sukuoneka, ndiye kuti zili bwino, apo ayi ndi Haraam. Ngati gawo limodzi la chinayi la chiwalo likhalabe losabisika mu Salah, ndiye kuti Salah sikhala yovomerezeka. (*Bahar-e-Shari'at, vol. 1, gawo 3, tsamba. 481*) Aliyense amene wavala Ihram pa Hajj kapena 'Umrah akuyenera kusamalira ichi kwakukulu.

13. Masiku ano, anthu ambiri amayendayenda atavala makabudula, kuwonetsa mawondo ndi tchafu zawo. Izi ndi Haraam. Kuyang'ananso mawondo ndi tchafu zowonetsedwazo za anthu amenewa zilinso Haraam. M'mbili mwa tsinje, malo amasewero komanso malo amasewero olimbitsa thupi ndimalo omwe izi zimaoneka kwambiri. Choncho, musamalitse pamene mucheza mmalo otere.

14. Chovala chomwe chimavalidwa posonyeza kudzikweza ndi choletsedwa. Ngati wina wadzikuza kapena ayi atha kutsimikizika pa kusinkhasinkha za makhalidwe ake. Ngati wina alichomwechi pa kuvala zovala zomwe ali nazo asanavale izi, zionetsa kuti iye sanakhale wozikuza. Ngati machitidwe am`mbuyo palibe izi, ziwonetsa kuti wayamba kuzikuza. Choncho, iye apewe kuvala zovala zotere chifukwa kuzikuza ndi khalidwe loipa.

(*Bahar-e-Shari'at, vol. 3, tsamba. 409; Rad-dul-Muhtar, vol. 9, tsamba. 579*)

Kuti muphunzire ma Sunnah zikwi pa mitu yosiyana siyana, gulani ndi kuwerenga ma buku a *Bahar-e-Shari'at* gawo 16, buku lamasamba 312, ndi *Sunnatayn aur Adaab*, buku la masamba 120, osindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah. Imodzi mwanjira zabwino kwambiri zophunzirira ma Sunnah yendani ndi Madani Qafilah ya Dawat-e-Islami pamodzi ndi odzipereka a mtumiki okonedwa.

*yendani ndi Qafila kuti mupeze Madalitso*  
*yendani ndi Qafila kuti muphunzire ma Sunnah*  
*yendani ndi Qafila ndipo mavuto anu adzatha*  
*yendani ndi Qafila mayeselo anu adzatha*

Okonedwa abale a Chisilamu! Pomaliza, ndikutengerapo mwayi uwu kutchula kupambana kwa ma Sunnah odala komanso ena mwa ma Sunan ndi makhalidwe. Mtumiki wa chifundo, opembedzera Ummah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ananena kuti, 'aliyense okonda Sunnah yanga, akonda ine, ndipo aliyense okonda ine adzakhala ndi ine mu Jannah.' (*Ibn-e-'Asakir, vol. 9, tsamba. 343*)

*upangeni Mtima wanga kukhala mzinda wa Sunnah zanu bwana*  
*ku Jannah zandipangeni kukhala moyandikana nanu*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ

## Ngale 17 za Madani zokhudza 'Imamah (chilemba)

Zonena zodala 6 za okonedwa Mustafa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ:

1. Ma Rak'aat awiri a Salah opempheredwa utavala 'Imamah ali bwino kuposa ma Rak'aat 70 opempheredwa opanda kuvala Imamah. (*Al-Firdaus bima Soor-il-Khitab, vol. 2, tsamba. 265, Hadith 3233*)
2. Kuvala 'Imamah pamwamba pa chisoti ku masiyanitsa pakati pathu ndi opembedza mafano. Pa kupinda kuli konse kwa Imamah komwe msilamu amamanga pozungulira mutu wake, iye adzapatsidwa Noor imodzi [kuwala] pa tsiku la chiweruzo. (*Al-Jami'-usSagheer, tsamba. 353, Hadith 5725*)
3. Mosakayikira, Allah عَزَّوَجَلَّ ndi angero ake amatumiza mafuno abwino lachisanu kwa iwo amene amavala 'Imamah. (*Al-Firdaus bima Soor-il-Khitab, vol. 1, tsamba. 147, Hadith 529*)
4. kupephera Salah mutavala 'Imamah ndikofanana ndi zabwino zokwana 10,000. (*Al-Firdaus bima' Soor-il-Khitab, vol. 2, tsamba. 406, Hadith 3805; Fatawa Razawiyyah, vol. 6, tsamba. 220*)
5. Pamene wina apemphera Salat-ul-Jumu'ah atavala 'Imamah, apeza zabwino zofanana ndi ma Salat-ul-Jumu'ah 70 opempheredwa asanavale 'Imamah.  
(*Tareekh-e-Madinah Dimashq li Ibn 'Asakir, vol. 37, tsamba. 355*)
6. Imamah ndi chipewa cha chifumu cha ma Arab, choncho valani Imamah ndipo ulemu wanu udzakulitsidwa. Aliyense omanga 'Imamah apeza ubwino pa kupinda

kulikonse [kwa ‘Imamah imene amamanga mozunguliza mutu wake]. (*Jam’-ul-Jawami, vol. 5, tsamba. 202, Hadith 14536*)

7. Zatchulidwa m`buku la masamba 1197 la Bahar-e-Shari’at, lofalitsidwa ndi Dawat-e-Islami nthambi yofalitsa, Maktaba-tul-Madinah, patsamba 660, voliyomu 3: Mangani ‘Imamah mutayimilira, ndikuvala chovala Buluku mutakhala pansu. Aliyense ochita mosutsana ndi ichi, iye adzavutika ndi nthenda, yomwe ilibe machiritso.
8. Musanayambe kumanga Imamah, khalani ndi chitsimikizo (Niya) chabwino. Ngati mulibe zolinga zabwino simupeza Sawab. pachifukwa ichi, khalani ndi cholinga ichi kuti” ine ndikumanga Imamah pakuchita Sunnah ndikukondweretsa Allah wamphamvu zonse”.
9. Ndikoyenera kukulunga moloza mbali ya manja yamutu pakupinda koyamba kwa ‘Imamah. (*Fatawa Razawiyyah, vol. 22, tsamba. 199*)
10. Shimlah [ mapeto osakulunga] yodalitsika ya ‘Imamah ya mtumiki wokonedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ nthawi zambiri imalendewera kumbuyo (ku msana wake wodala), nthawi zina umakhala kumbali kwa dzanja lake lamanja, ndipo nthawi zina amakhala ndi ma Shimlah awiri pakati pa mapewa ake odala. Kulendeweletsa Shimlah kumbali ya dzanja la manzere ndikotsutsana ndi Sunnah. (*Ashi’a-tul-Lam’aat, vol. 3, tsamba. 582*)

11. Kutalika kwa Shimlah ya Imamah kukhale kofanana ngati zala zinayi mulifupi, ndi kufikira pakati penipeni pa msana, monga kutalika kwa nkono.

*(Fatawa Razawiyyah, vol. 22, tsamba. 182)*

12. Mangani Imamah mutayima cholunjika ku Qiblah. *(Kashf-ul-Iltibas, tsamba. 38)*

13. Sunnah ya Imamah ndi yoti isakhale yofupika kuposa mayadi awiri ndi theka mukutalika kwake, komanso isakhale yayitali kuposa mayadi asanu ndi limodzi, ndipo limangidwe mmaonekedwe a domu. *(Fatawa Razawiyyah, vol. 22, tsamba. 186)*

14. Ngati muli ndi mpango wawukulu omwe mungathe kuzunguliza mokwanira kubisa mutu wonse, iyi itengedwa ngati Imamah.

15. Ndi Makruh kumanga mpango wochepa omwe utha kupanga mfundo imodzi kapena ziwiri zokha.

*(Fatawa Razawiyyah, vol. 7, tsamba. 299)*

16. Pamene mukufuna kumanganso 'Imamah kachikena masulani mfundo imodzi imodzi mmalo mongovula yonse pakamodzi ndi kuyiponya pansu. *(Fatawa Hindiyyah, vol. 5, tsamba. 330)*

17. Ngati yachotsedwa pachifukwa chenicheni ndipo iwe ukufuna kuyimanganso ndiye kuti tchimo limodzi lichotsedwa pakumasula mfundo imodzi imodzi.

## Chonde werengani mfundo 6 za a zaumoyo zakupindulitsa kwa ‘Imamah

1. Tsitsi la anthu amene akhala ndi mutu osafunda liri pa chiopsezo cha zotsatira ku nyengo yozizira, chilimwe ndi dzuwa. Izi sizononga tsitsi lokha komanso ubongo ndi nkhope ndipo zitha kuononga thanzi la munthu. Ngati munthu amavala Imamah ndicholinga chotsata Sunnah, ndizaphindu pano pa dziko lapansi ndi kudziko liri nkudza.
2. Molingana ndi kafukufuku wazachipatala, kuvala Imamah ndikopindulitsa kwambiri ku matenda a mutu.
3. Imamah imalimbitsa ubongo ndi kukumbukira.
4. Kuvala Imamah kumateteza munthu ku chimfine, ngati ovalayo akudwala chimfine, zotsatira zake ndizochepa.
5. Shimlah ya Imamah imateteza ku kupuwala kwa ziwalo za gawo lathupi lakumusi, chifukwa Shimla imapereka chitetezo cha msana ku zotsatira za nyengo monga, nthawi yozizira, chilimwe ndi zina.
6. Shimlah imachepetsa chiopsezo cha “سرسام”. (Nthenda yakutupa kwa ubongo imatchedwa “سرسام”).

‘Allamah Shaykh ‘Abdul Haq Muhaddis Dihlvi رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ ananena kuti: ‘Imamah yodalitsika ya mtumiki wolemekezeka

صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ nthawi zambiri inali ya mtundu woyera, nthawi zina yokuda, ndi thawi zinanso wobiriwira.’ (*Kashf-ul-Iltibas, tsamba. 38*)

صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ! الْحَمْدُ لِلَّهِ عَزَّوَجَلَّ Mtumiki wolemekezeka anavalaponso Imamah wobiriwira. Ndipo ndi mtundu wanji wabwino wobiriwira! Chimphika chodala cha pamwamba pa Mzikiti wopatulika wa Mtumiki wathu wokonedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ chilinsu chobiriwira.

Njira yabwino yophunzirira Sunan ndikuyenda pamodzi ndi olimbikitsa ma Sunnah a Madani Qafilah ya Dawat-e-Islami.

*kuwala kwa dzuwa ndi mwedzi sikukufunika m’madinah  
kumeneko kuwala kwa chimphika cha Girini chimakwanira Usiku ndi  
Usana*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Kuti muphunzire ma Sunnah zikwi pa mitu yosiyana siyana, gulani ndi kuwerenga ma buku a *Bahar-e-Shari’at* gawo 16, buku lamasamba 312, ndi *Sunnatayn aur Adaab*, buku la masamba 120, osindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah. Imodzi mwanjira zabwino kwambiri zophunzirira ma Sunnah yendani ndi Madani Qafilah ya Dawat-e-Islami pamodzi ndi odzipereka a mtumiki okonedwa. (Arabic`)

*yendani ndi Qafila kuti mupeze Madalitso  
yendani ndi Qafila kuti muphunzire ma Sunnah*

*yendani ndi Qafila ndipo mavuto anu adzatha  
yendani ndi Qafila mayeselo anu adzatha*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Okonedwa abale a Chisilamu! Pomaliza, ndikutengerapo mwayi uwu kutchula kupambana kwa ma Sunnah odala komanso ena mwa ma Sunan ndi makhalidwe. Mtumiki wa chifundo, opembedzera Ummah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ananena kuti, ‘aliyense okonda Sunnah yanga, akonda ine, ndipo aliyense okonda ine adzakhala ndi ine mu Jannah.’ (*Ibn-e-Asakir, vol. 9, tsamba. 343*)

*upangeni Mtima wanga kukhala mzinda wa Sunnah zanu bwana  
ku Jannah zandipangeni kukhala moyandikana nanu*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

## Ngale 19 za Madani zokhudza mphete

1. Ndi Haraam kuti mwamuna avale mphete ya golide. Mtumiki okonedwa ndi Odalitsika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ analetsa kuvala phete ya golide. (*Sahih Bukhari, vol. 4, tsamba. 67, Hadith 5863*)
2. Ndi Haraam kukhala ndi wachichepere (mnyamata) wovala zozikongoletsera zopangidwa ndi golide ndi siliva, ndipo iye wokhala ndi wachichepere wochita izi akhala ochimwa. Mkazi atha kupaka henna mmanja ndi mapazi ake, koma ngati apaka izi kwa mnyamata, iye akhala



ochimwa. (*Bahar-e-Shari'at, vol. 3, tsamba. 428; Durr-e-Mukhtar, Raddul-Muhtar, vol. 9, tsamba. 598*) palibe choipa kupaka henna m'manja ndi mapazi a wachichepere (wamkazi).

3. Mphete ya chitsulo ndi chokongoletsa cha iwo owonongedwa (okhala ku gahena). (*Jami' Tirmizi, vol. 3, tsamba. 305, Hadith 1792*)
4. Ndikoloredwa amuna kuvala phete yachimuna yokha monga imene ili ndi mwala okongola umodzi. Ngati ili ndi miyala yokongola kuposa umodzi kapena miyala yokongola ilipo yambiri, choncho siziri zololedwa kwa amuna ngakhale zapangidwa ndi siliva. (*Rad-dul-Muhtar, vol. 9, tsamba. 597*)
5. Ndikosaloredwa [kwa amuna] kuvala mphete yopanda mwala okongola pakuti yopanda mwala okongola simatengedwanso ngati mphete.
6. Ndikoloredwa kuvala mphete yolembedwa Huroof-e Muqatta'at [malemba oyambirira a ma Surah a mu Qur'an] koma ndikosaloredwa kuvala kapena kukhudza mphete imeneyi ulibe Wuzu. Momwemonso, sikoloredwa kwa iye wogwilana chanza ndi uyo wovala mphete yotere kukhudza mpheteyo opanda Wuzu.
7. Chimodzimidzi, ndikosaloredwa kuti amuna avale kuposera mphete imodzi (yoloredwa). Akazi atha kuvala mphete yopanda mwala okongoletsa.

(*Bahar-e-Shari'at, vol. 3, tsamba. 428*)

8. Ngakhale palibe kufunikira kogwilitsa ntchito mphete ngati chidindo, ndikoloredwa kuvala mphete ya siliva yolemera kuchepera 4.5 Masha (4galamu ndi 374 miligalamu) ndipo ili ndi mwala umodzi wokha okongola. Komabe, kwa iye amene sakufuna kuyigwiritsa ntchito ngati chidindo chovomerezeka, ndikofunika kusavala angakhale mpheteyo ndiyo- loredwa. Kwa iye amene akufuna kugwiritsa ntchito ngati chidindo chovomerezeka, sikuvomerezeka kokha komanso ndi Sunnah kuvala mtundu wa mphete umenewu pa chifukwa chomwechi. komabe, ngati wina avala ndikumaonetsa kudzikuzi kapena kutengera machitidwe achikazi kapena ndimalingariri aliwonse oyipa, Ndiye kuti sizoloredwa kuvala angakhale zovala zokongola. (*Fatawa Razawiyyah, vol. 22, tsamba. 141*)
9. Ndikofunika kuvala mphete pa mwambo wa Eid koma amuna atha kuvala yoloredwa yokha basi.
10. Kuvala mphete ndi Sunnah kwa iwo wokha akufuna kugwilitsa ntchito ngati chidindo chovomerezeka, ngati Mfumu, ma Qadi ndi ma Mufti kudinda Fatawa (ndi mphete). Kupatula anthu awa, sisunnah kwa iwo amene sakufuna kuyigwiritsa ntchito monga chidindo chovomerezeka ngakhale zilizoloredwa kuvala. (*Fatawa 'Aalamgiri, vol. 5, tsamba. 335*)

mphete sizikugwilitsidwanso ntchito ngati chidindo koma chidindo chapadera chikugwilitsidwa pa cholinga chimenechi.

Chifukwa chake, sisunnah kuvala mphete ingakhale chifukwa cha ma Qadi ndi ena, amene safuna kugwiritsa tchito ngati chidindo.

11. Amuna avale mphete munjira yoti mwala wamtengo wapatali ukhalebe ukuloza ku chikhatho pamene akazi ayenera kuyika mwalawo kumbuyo kwadzanja.

*(Al-Hidayah, vol. 4, tsamba. 367)*

12. Mphete yopanda mwala wamtengo wapatali ndiyofanana ndi zokongoletsa za chikazi, ndipo kwa amuna, ndi Makruh (Tahrimi, zosaloredwa ndinso tchimo). *(Fatawa Razawiyyah, vol. 22, tsamba. 130)*

13. Akazi atha kuvala mphete zambiri za siliva ndi golide monga akondera kaya ndi mwala wamtengo wapatali kapena ayi. Kwaiwo palibe malire a kulemera kwa siliva ndi golide ndi kuchuluka kwa miyala.

14. Ngati mphete ya chitsulo yakutidwa ndi siliva kotero chitsulo sichikuoneka, sizilizoletsedwa (kwa onse amuna ndi akazi) kuvala mphete yotere. *(Fatawa 'Aalamgiri, vol. 5, tsamba. 335)*

15. Munthu atha kuvala mphete pa dzanja lililonse koma avale pachala chaching`ono. *(Rad-dul-Muhtar, vol. 9, tsamba. 596)*

16. Ndikosavomerezedwa ndinso tchimo kuti amuna avale

chibangili cha chitsulo kapena chofanana ndi Mannat kapena Dam.

17. Momwemonso, ndikosavomerezedwa kuvala mphete yopanda mwala yopangidwa ndi siliva kapena chitsulo chilichonse, kapena mphete yachitsulo yobweretsedwa kuchokera ku Madinah Munawwarah **رَأَاهَا اللَّهُ شَرِّقًا وَتَعْظِيمًا** kapena Ajmer.
19. Sizovomerezedwanso kuti amuna avale mphete yopanda mwala yopangidwa kuchokera ku siliva kapena chitsulo chilichonse pomwe kuuzira zina la Allah kwapangidwa, kuchiza kuotcha ndi kutupa kwa Nsempha wa pa chokhalira komwe kumayambitsa kutuluka magazi ndi matenda ena.
20. Ngati m`bale wa chisilamu wavala chibangili chopangidwa ndi chitsulo kapena mphete yopanda mwala, kapena tcheni, kapena mtundu uliwonse osavomerezeka wamphete, iye ndiwokakamizidwa ndi Shari`ah nthawi yomweyo kuchotsa, ndikulapa kwa Allah **عَزَّوَجَلَّ** ndikupanga chiganizo cholimba kuti sadzavalanso. Ndipo osampatsa m`bale wina aliyense wa chisilamu kuti avale.

Kuti muphunzire ma Sunnah zikwi pa mitu yosiyana siyana, gulani ndi kuwerenga ma buku a *Bahar-e-Shari`at* gawo 16, buku lamasamba 312, ndi *Sunnatayn aur Adaab*, buku la

masamba 120, osindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah. Imodzi mwanjira zabwino kwambiri zophunzirira ma Sunnah ndi yendani ndi Madani Qafilah ya Dawat-e-Islami pamodzi ndi odzipereka a mtumiki okondedwa.

*yendani ndi Qafila kuti mupeze Madalitso*  
*yendani ndi Qafila kuti muphunzire ma Sunnah*  
*yendani ndi Qafila ndipo mavuto anu adzatha*  
*yendani ndi Qafila mayeselo anu adzatha*

صَلُّوا عَلَيَّ الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَيَّ مُحَمَّدٍ

Okondedwa abale a Chisilamu! Pomaliza, ndikutengerapo mwayi uwu kutchula kupambana kwa ma Sunnah odala komanso ena mwa ma Sunan ndi makhalidwe. Mtumiki wa chifundo, opembedzera Ummah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ananena kuti, aliyense okonda Sunnah yanga, akonda ine, ndipo aliyense okonda ine adzakhala ndi ine mu Jannah.’ (*Ibn-e-Asakir, vol. 9, tsamba. 343*)

*upangeni Mtima wanga kukhala mzinda wa Sunnah zanu bwana*  
*ku Jannah zandipangeni kukhala moyandikana nanu*

صَلُّوا عَلَيَّ الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَيَّ مُحَمَّدٍ

## **Ngale 20 za Madani zokhudza Miswak (Mswachi wantengo)**

Poyamba, zonenadwa ziwiri zodalitsika za wolemekezeka Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ zaperekedwa pansipa:

1. Ma Rak'at awiri opempheredwa utatha kuchita Miswak ali bwino kuposa ma Rak'at 70 opempheredwa opanda kuchita Miswak. (*Attargheeb Wattarheeb, vol. 1, tsamba. 102, Hadith 18*)
2. Khazikitsani mwa inu nokha kugwiritsa tchito Miswak chifukwa ndi choyambitsa kuyera pakamwa ndi kusangalatsa Allah عَزَّوَجَلَّ  
(*Musnad Imam Ahmad, vol. 2, tsamba. 438, Hadith 5869*)
3. Patsamba 288 la voliyomu yoyamba ya Bahar-e-Shari'at, lofalitsidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yosindikiza ya Dawat-e-Islami, 'Allamah Maulana Mufti Muhammad Amjad 'Ali A'zami رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ ananena kuti: ophunzira wolemekezeka akuti, iye amene amagwilitsa ntchito Miswak kawirikawiri, adalitsika ndi kuwerenga Kalimah pa nthawi ya kumwalira kwake, ndipo iye amene amatenga mankhwala osokoneza bongo sadzadalitsika ndi kuwerenga Kalimah pa nthawi yakumwalira kwake.
4. Sayyiduna Ibn 'Abbas رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا ananena kuti Miswak uli ndi maubwino khumi: umayeletsa mkamwa, umalimbitsa msinini, maso amaona bwino, umachotsa chifuwa (phlegm), umachotsa mphweya woyipa, ndi kusunga Sunnah, angelo amakhala okondwera, Allah عَزَّوَجَلَّ amasangalala, umaonjezera makhalidwe abwino ndi kuonjezera kagwilidwe kabwino ka m`mimba. (*Jam`ul-Jawami', vol. 5, tsamba. 249, Hadith 14867*)

5. Sayyiduna ‘Abdul Wahhab Sha’rani رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ Ananena kuti: Sayyiduna Abu Bakr Shibli Baghdadi رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ kamodzi, anafuna Miswak pamene anachita Wuzu. Iye anayang’ana koma sanathe kuupeza. Choncho iye رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anagula Miswak ndi dinar imodzi (khobidi la golide) ndikugwiritsa tchito. Anthu ena ananena naye, ‘iwe waononga zambiri pa ichi! Kodi munthu awononge zambiri pa Miswak?’ رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anayankha, ‘mosakayikanso, dziko ili ndi zonse zomwe zikhalamo sizamtengo ofanana ndi mapiko a udzudzu pamaso pa Allah عَزَّوَجَلَّ. Ndiyankha bwanji ngati patsiku la chiweruzo, Allah عَزَّوَجَلَّ Akandifunse, ‘chifukwa chani unasiya Sunnah (Miswak) ya Mtumiki wanga wokonedwa صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ? Choonadi cha ndalama ndi chuma chomwe ndinakupatsa iwe sizikufanana ndi mapiko a udzudzu, izi zili choncho, chifukwa chani sunawononge chuma chosafunikirachi pokwaniritsa Sunnah yopambana (Miswak)?’ (*Kuchokera mu: Lawaqa-ul-Anwaar, tsamba. 38*)
6. Sayyiduna Imam Shaafi’i رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ Ananena kuti, ‘zinthu zinayi zimalimbikitsa luntha: kudziretsa ku kucheza kosathandiza, kugwiritsa Miswak, kukhala pamodzi ndi anthu opemphera ndi kuchita mogwirizana ndi [chipembedzo] chidziwitso chanu.’  
(*Hayat-ul-Haywan, vol. 2, tsamba. 166*)
7. Miswak ikuyenera kuchokera ku mtengo wa Pilu, azitona, kapena Nimu wokhala ndi makomedwe owawa.

8. Makulidwe a Miswak ayenera kukhala chimodzimidzi ndi a chala chaching'ono.
9. Miswak sikuyenera kukhala yotalika kuposa dzanja limodzi. Kupanda kutero, Satana amakhala pamenepo.
10. Misisi a Miswak ziyenera kukhala zofewa. Kupanda kutero zimapangitsa mipata pakati pa mano ndi nsinini.
11. Ngati Miswak ali wamuwisi, ndi zabwino kwambiri. Ngati siwamuwisi viyikani mu mutambula lamadzi kuti afewe.
12. Ndikoyenera kuchepetsa misisi ya Miswak tsiku ndi tsiku chifukwa amapindulitsa ngati akhalabe owawa mmakomedwe.
13. Tsukani mano anu ndi Miswak mopingasa.
14. Nthawi iliyonse mugwilitsa tchito Miswak, gwilitsani katatu.
15. Ndipo mudzimutsuka nthawi iliyonseyo.
16. Gwirani Miswak kudzanja la manja mu khalidwe loti chala cha ching'ono chikhalebe pansu, ndi zala zitatu zapakati zikhalebe pamwamba pake, pamene chala chachikulu chikhale pamwamba (pafupi ndi misisi yofewa yomwe ikugwilitsidwa potsuka mano).
17. Poyamba tsukani (ndi Miswak) mano akumwamba mbali ya manja kenako ya ma mzere. Pambuyo pake, tsukani



mano a m`musi kuyambira mbali yakumanja kenako yakumanzere.

18. Kugwilitsa ntchito Miswak pogwira msonga kumabweretsa chiopsezo cha kuotcha ndi kutupa kwa Nsempha wa pa chokhalira komwe kumayambitsa kutuluka magari.
19. Miswak ndi Sunnah muzichita musanapange Wuzu, koma ngati wina ali ndi fungo lonunkha mkamwa, ndiye kugwiritsa ntchito Miswak kumakhala Sunnat-ul-Muakkadah.

*(Kuchokera mu: Fatawa Razawiyah, vol. 1, tsamba. 623)*

20. Musataye Miswak wogwiritsidwa tchito kale popeza ndi chida chogwiritsidwa ntchito pa Sunnah. M`malo mwake, sungani malo wena awulemu, kwirirani kapena ponyani M`nyanja mutatha kuimangirira ku mwala pena kuchithu cholemera. ndi zina zotero *(kuti mumve zambiri werengani pasamba 294 ndi 295 a Bahar-e-Shari`at, vol. 1, losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah)*

Kuti muphunzire ma Sunnah zikwi pa mitu yosiyana siyana, gulani ndi kuwerenga ma buku a *Bahar-e-Shari`at* gawo 16, buku la masamba 312, ndi *Sunnatayn aur Adaab*, buku la masamba 120, osindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah. Imodzi mwanjira zabwino kwambiri zophunzirira ma Sunnah

yendani ndi Madani Qafilah ya Dawat-e-Islami pamodzi ndi odzipereka a mtumiki okonededwa. (صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ)

*yendani ndi Qafila kuti mupeze Madalitso  
yendani ndi Qafila kuti muphunzire ma Sunnah*

*yendani ndi Qafila ndipo mavuto anu adzatha  
yendani ndi Qafila mayeselo anu adzatha*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Okonededwa abale a Chisilamu! Pomaliza, ndikutengerapo mwayi uwu kutchula kupambana kwa ma Sunnah odala komanso ena mwa ma Sunan ndi makhalidwe. Mtumiki wa chifundo, opembedzera Ummah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ananena kuti, ‘aliyense okonda Sunnah yanga, akonda ine, ndipo aliyense okonda ine adzakhala ndi ine mu Jannah.’ (*Ibn-e-Asakir, vol. 9, tsamba. 343*)

*upangeni Mtima wanga kukhala mzinda wa Sunnah zanu bwana  
ku Jannah zandipangeni kukhala moyandikana nanu*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

## Ngale 16 za Madani Poyendera manda

1. Mtumiki okonededwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ananena kuti, ‘ine ndinali kukuletsani kuyendera manda, koma tsopano, inu muyenera kuyendera manda, chifukwa izi zimabweretsa

kusakhuzidwa ndi za pa dziko lapansi n di kum'panga wina kukumbukira zatsiku lomaliza.'

*(Sunan Ibn Majah, vol. 2, tsamba. 252, Hadith 1571)*

2. Kuyendera manda a silamu ndi Sunnah ndipo ndi chamwayi waukulu kuyendera Manda olemkezeka a ma Awliya Allah رَحْمَةُ اللَّهِ dalitsika ndi a anthu ofera mnjira ya Allah رَحْمَةُ اللَّهِ, kuwachitira Isal e Sawab (kutumiza mphoto) ndi kokonedwa komanso ndimachitidwe opedzera mphoto. *(Fatawa Razawiyyah, vol. 9, tsamba. 532)*
3. Ngati aliyense akufuna kuyendera manda a msilamu (kapena kachisi odalitsika wa woyera mtima aliyense رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ), ndizokonedwa kupemphera ma Rak'aat awiri a salah ya Nafl ali kunyumba kwake koma osati mu nthawi yoletsedwa. Mu Rak'aat iliyonse, iye akuyenera kuwerenga Ayatul-Kursi kamodzi kenako Surah Al-Ikhlash katatu pambuyo pa Surah Al-Fatihah. Salah iyi iye akuyenera kuchita Isal e Sawab kwa akufa ali ku manda. Allah عَزَّوَجَلَّ adzalenga Noor (kuwala) m'manda awakufa ndi kupereka mphoto zazikulu kwa munthu ameneyu (monga opanga Isal e Sawab). *(Fatawa 'Aalamgiri, vol. 5, tsamba. 350)*
4. Aliyense oyendera Manda wodalitsika kapena manda awamba, sayenera kuzitangwanitsa ndi kulankhula zosayenera munjira mwake. *(Fatawa 'Aalamgiri, vol. 5, tsamba. 350)*

5. Musapsopsone manda kapena kuyika manja anu pamenepo. (*Fatawa Razawiyyah, vol. 9, tsamba. 522, 526*) mmalo mwake, Imani patali pang`ono ndi manda.
6. Kuchita Sajdah pa manda ndi Haraam, ndipo ngati mwapanga ndi cholinga cha ku pembedza, ndi Kufr (kusakhulupirira). (*Kuchokera mu: Fatawa Razawiyyah, vol. 22, tsamba. 423*)
7. Gwiritsani ntchito njira yodziwika ku manda komwe kunalibe manda a chisilamu m`mbuyomu. Osayenda panjira yopangidwa kumene.

Izi zikunenedwa mu Rad-dul-Muhtar: ndi Haraam kuyenda pa njira ya tsopano yopangidwa (pakugumula manda pamanda).’ (*Rad-dul-Muhtar, vol. 1, tsamba. 612*) zoona zake, ngakhale pali kukayika kokhudzana ndi njira yatsopano, ndikosaloredwa komanso ndi tchimo kuyendamo. (*Durr-e-Mukhtar, vol. 3, tsamba. 183*)

8. Zakhala zikuoneka mmalo ambiri a Manda opaturika a oyera mtima ndi cholinga chothandiza alendo, kumapangidwa ngalande za tsopano ndi misewu pokugumula manda a asilamu. Ndi Haraam kugona, kuyenda, kuyima, ngakhale kukhala pansu ndi zina zotero, kuti muthe kuchita Zikr kapena kuwerenga qur’an. Fatiha iyenera kuwerengedwa kuchokera patali.
9. Alendo ayenera kuyima kutsogolo kwa nkhope ya munthu oyikidwayo. Iye ayenera kubwera pafupi ndi manda

kuchokera kumbali ya mapazi amunthu oyikidwa, ndi cholinga choti iye akhale pamaso pa munthu oyikidwa. Iye sakuyenera kubwera ku chokera kumbali ya mutu wa omwalira ndi cholinga choti omwalira ayimike mutu wake kuti a wone alendo. (*Fatawa Razawiyyah, vol. 9, tsamba. 532*)

10. Imani m`manda munjira yoti msana wanu waloza Qiblah ndipo nkhope yanu yaloza nkhope za okhala m`manda. Kenako, nenani:

السَّلَامُ عَلَيْكُمْ يَا أَهْلَ الْقُبُورِ يَغْفِرُ اللَّهُ لَنَا وَلَكُمْ أَنْتُمْ سَلَفْنَا وَنَحْنُ بِالْآتِ

**Kumasulira:** mtendere ukhale kwa inu, E anthu a M`manda! Allah akhululukire ife ndi inu. Mwabwera kuno patsogolo pathu ndipo ife tikutsatirani.

(*Fatawa 'Aalamgiri, vol. 5, tsamba. 350*)

11. Aliyense wolowa m`manda ndikuwerenga Du'a iyi:

اللَّهُمَّ رَبَّ الْأَجْسَادِ الْبَالِيَةِ وَالْعِظَامِ النَّخِرَةِ الَّتِي خَرَجَتْ مِنَ الدُّنْيَا وَ  
هِيَ بِكَ مُؤْمِنَةٌ أَدْخِلْ عَلَيْهَا رَوْحًا مِنْ عِنْدِكَ وَسَلَامًا مِنِّي

**Kumasulira:** E Allah *عَزَّوَجَلَّ* mbuye wa matupi amene alowa nthakayi ndi mafupa amene awonongeka! Perekani chifundo chanu kwa iwo achoka padziko ali muchikhulupiriro chanu ndipo apatseni iwo mtendere kuchokera kwa ine.

Choncho onse okhulupirira, amene anamwalira kuchokera nthawi ya Sayyiduna Aadam عَلَيْهِ السَّلَام kufikira nthawi ya pempholi, adzapanga Du'a ya chi khululuko kwa amene wachita Du'a iyi. (*Musannaf Ibn Abi Shaybah, vol. 8, tsamba. 257*)

12. Mtumiki okondedwa صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ananena: ngati munthu alowa m'manda, awerenge Surah Al-Fatihah, Surah Al-Ikhlās ndi Surah At-Takasur kenako iye apemphe, E Allah! Chili chonse ndawerenga mu Qur'an, perekani Sawabu zake kwa ma Mu'min amuna ndi akazi a m'mandamu, ndipo onse okhulupirira adza khala (otumiza Sawabu) ankhala pakati ake pa tsiku la chiweruzo. (*Sharh-us-Sudoor, tsamba. 311*)

13. Zanededwa mu Hadith yodalitsika: aliyense owerenga Surah Al Ikhlas ka 11 ndi kutumiza mphotho yake kwa anthu omwalira, iye apeza Sawab (mphotho) mofanana ndi kuchuluka kwa anthu omwalira. (*Durr-e-Mukhtar, vol. 3, tsamba. 183*)

14. Musayatse lubani pamanda pakuti ndikupanda ulemu komanso zosangalatsa. Ngati kununkhira kosangalatsa kupangidwa chifukwa cha alendo, ndiye lubani ayatsidwe pa malo osakhaliidwa patali ndi manda, pakuti kufalitsa kununkhira kosangalatsaku ndi chithu chosakhala bwino.

(*Fatawa Razawiyah, vol. 9, tsamba. 482, 525*)

15. A'la Hazirat (رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ) ananena pa malo ena kuti:

zinalankhulidwa ndi Sayyiduna ‘Amir Bin ‘Aas رَضِيَ اللهُ عَنْهُ mu buku la Sahih Muslim kuti pa nthawi ya imfa yake, Sayyiduna Amir Bin Aas رَضِيَ اللهُ عَنْهُ analangiza mwana wake wa mmuna, Pamene Ndamwalira palibe mkazi wolira kapena kuperekezedwa ndi moto (*Sahih Muslim, pp. 75, Hadith 192*)

16. Musayike nyali yamafuta kapena kandulo loyatsa ndi zina zotere pa manda. Ngati cholinga cha kuwala chapangidwira oyenda pansu usiku, choncho mutha kuyika kandulo kapena nyali ku mbali imodzi yamanda.

Kuti muphuzire ma Sunnah zikwi pa mitu yosiyana siyana, gulani ndi kuwerenga ma buku a Bahar-e-Shari’at gawo 16, buku lamasamba 312, ndi Sunnatayn aur Adaab, buku la masamba 120, osindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah. Imodzi mwanjira zabwino kwambiri zophunzirira ma Sunnah yendani ndi ma Qafilah a Madani a Dawat-e-Islami pamodzi ndi odzipereka a mtumiki okondedwa.

*yendani ndi Qafila kuti mupeze Madalitso*  
*yendani ndi Qafila kuti muphuzire ma Sunnah*  
*yendani ndi Qafila ndipo mavuto anu adzatha*  
*yendani ndi Qafila mayeselo anu adzatha*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

### Kukhala msilamu woopa mulungu ndi wopemphera Salah

Khalani usiku onse mu ijtima ya Dawat-e-Islam yolimbikitsa sunna yomwe imachitika lachinayi sabata iliyonse pambuyo pa salat-ul-maghrif m'dera lanu, chifukwa chomusangalatsa Allah ﷻ, ndi zolinga zabwino. Kuti muphunzire ma Sunnah, chipangeni kukhala chizolowezi chanu choyenda ndi Madani Qafilah masiku atatu mwezi uliwonse pamodzi ndi odzipereka a Rasool, kumalizitsa kulemba mkabuku ka Madani In'amaat tsiku lilonse kuchita fikr-e-Madina ndikukapereka kwa m'bale wachisilamu woyenera yemwe ali ndi udindo mdera lanu tsiku loyamba la mwezi uliwonse wa Madani.

#### Cholinga changa cha madani

Ndiyenera kuyesetsa kudzikonza ndekha ndi anthu apadziko lonse lapansi, ﷺ. Ndicholinga choti tidzisinthe tokha, tiyenera kuchitapo kanthu pa Madani In'amaat ndikuyesetsa kusintha anthu a dziko lonse lapansi, tiyenera kuyenda ndi Madani Qafilah ﷺ.



Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagaran  
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

UAN: +92 21 111 25 26 92 | Ext: 7213

Web: [www.dawateislami.net](http://www.dawateislami.net) | E-mail: [translation@dawateislami.net](mailto:translation@dawateislami.net)